# African Bat Conservation – Kunena za Corona Virus (Coronavirus Statement)

www.africanbatconservation.org

Moyetsetsa a malawi akukakamizidwa kupewa kufara kwa kachilombo ka corona virus ( SARS-CoV-2) ndi matenda a corona virus (COVID-19). African bat conservation ikufuna ikupaseni chilungamo chokhuza matenda a coronavirus (COVID-19) ndi mileme.

1. **Mileme simafalitsa corona virus, koma anthu ndi amene amapatsirana okha okha.**

2. **Palibe umboni weni weni oti mileme imapasira anthu kachilombo ka SARS-CoV-2.**

   Pakadalipano sitikuziwa kwenikweni mene tizilombo ta SARS-Cov-2 tinachokera mu nyama kulowa m'matupi mwa anthu. Kafukufuku yemwe anatulusidwa mu Januwale 2020 pa bioRxiv.org ndi athu ochita akafukufuku ku wuhan insituti yophuzira zama virus udaonesa kuti tizilombo ta SARS-CoV-2 timagawa 96 perecenti yama jinomu ake ndi SARS ngati coronavirus. (Zhou et al. 2020). Kwenikweni mileme ya Rhinolophid ( horseshoe) ku china ndiimene imasunga tizilombo ta SARS tofanana ndi coronavirus, ngakhale mtundu wina " wapakatitikati "ukhoza kukhala umatha kupasila athu (Lam et al. 2020). Nyama zambili zimakhala ndi coronavirus komaso zili ndikuthekera kokhala ndi gwero la matenda.

3. **Kupha mileme sikungalepherese kufara kwa tizilombo ta SARS-Cov-2.**

   Kuli ma lipoti ambili omwe m'madera komaso malamuro aboma mu zigawo zosiyana siyana mu dziko la pansi omwe amapangisa kuti mileme ichosedwe pothana ndi matenda. Choncho **kupha mileme nthawi ino ya mlili ndi kolakwika** kuononga malo okhala mileme sikungachite chilichose pochepesa chiopsezo ndipo sitingachepese chiopsezo pokupha nyama za tchile.

4. **Mileme ili ndi ubwino osaneneka ngati kupangisa kuti zipaso zibereke, kugawikana/kumwazikana kwa mbeu ndiku kuteteza mbeu kutizilombo toononga. Kupha mileme kuli ndikuthekera kolepheretsa kasungidwe ndi ubwino wa mileme ku anthu.**

5. **Mileme yonyamula kachilombo ko yambisa matenda a corona virus siopsa ku moyo wa munthu ngati anthu salimbana nayo.** Kafukufuku waonesa kuti nambala ya mitundu ya mileme, kweni kweni malo otetha ndi malo omwe amakhala ma virus ndi tizilombo tina tomwe timatha kuyambisa matenda opasilana kwa anthu ngati nipah virus, SARS ndi Ebola. Choncho ma virus anabwera mochuluka chifukwa cha mchitidwe wa anthu omwe unapangisa kusintha kwa chilengedwe omwe umabweresa mileme, anthu ndi ziweto pamozi. Izi zimachitika pomwe anthu amakalowa kapena kusokoneza malo omwe imakhala mileme mwachitsanzo kudula mitengo wachisawawa kapena malo omwe imasaka ndikudya mileme.

   Pali mitundu 1400 ya mileme yomwe imakhala tchile pa dziko la pansi. yambili inazolowera nyengo yamatauni, imakhala m'minda yapakhomo, ku denga, m'mapaki a ntauni kumaso imatha kukhala pansi pa mlatho, popanda kupereka chiopseza kwa anthu oyandikanana nao.

Mkulu wa misonkhano yoteteza mitundu ya nyama za m'tchire ndi zoyendayenda anati **"njira yomwe tingapange pothana ndi kachilombo ka SARS-CoV-2 ndikuletsa mchitidwe ofalisa, umene uli ochokera ku athu kupita ku athu. Kwa nthawi yayitali, tikuyenera kuyesa ndikulesa mchitidwe ogwilisa ntchito nyama zakutchire ndikuononga malo achilengedwe kuti tipewe zochitika zoipa mtsogolo."**

*Chilungamochi chikutengera pa zomwe anakonza a Bat Conservation International, Bat Conservation Trust, the Secretariats of the Convention on the Conservation of Migratory Species of Wild Animals (CMS), the Agreement on the Conservation of Populations of European Bats (EUROBATS), the Agreement on the Conservation of African-Eurasian Migratory Water birds (AEWA) and the Eco Health Alliance.

**MAUMBONI**

Lam T, Shum M, Zhu H, Tong Y, Ni X, Liao Y. et al. Identification of 2019-nCoV related coronaviruses in Malayan pangolins in southern China. BIORXIV. 2020 doi: 10.1101/2020.02.13.945485.

Zhou P, Yang XL, Wang XG, Hu B, Zhang L, Zhang W, A pneumonia outbreak associated with a new coronavirus of probable bat origin. Nature. 2020.